Baibulo ya ana
Ikupasilani

# Yesu Adyetsa Anthu 5,000

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Janie Forest
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Ruth Klassen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Atsogoleri achipembedzo ambiri (otchedwa Afarisi) ankanena zabodza zokhudza Yesu. Ena anayesanso kumupha.

Iwo sanakhulupirire kuti Iye analidi Mwana wa Mulungu. Iwo sanamulandire ngakhale kuti anachita zozizwitsa zimene Zinatsimikizira kuti iye ndi Mwana wa Mulungu.

Tsiku lina Yesu anawoloka nyanja ya Galileya. Mwina ankafuna kupuma pang'ono kuchokera kwa makamu omwe ankasonkhana momuzungulira Iye. Koma khamu la anthu posakhalitsa linampeza Iye. Iwo akhadziwa kuti Yezu akhacita pirengo pikulu. Iwo ankafuna kuti akhale ndi Iye.

Yesu anatsogolera ophunzira ake kuphiri lachipululu kumene Iye anakhala akuphunzitsa. Anthu ochulukirachulukira anapitiriza kubwera. Posakhalitsa inali nthawi ya mgonero. Aliyense a yenera kuti anali ndi njala.

Yesu anayang'ana khamulo. Tidzagula kuti mikate kuti adye awa? Anafunsa Filipo. Panalibe malo ogulitsira zakudya. Kodi Yesu ankafuna kuchita chiyani?



Filipo anayankha Yesu kuti: “Ndi ndalama zambiri kudyetsa khamu ili.” Yesu ndi ophunzira ake analibe ndalama zambiri.



Wophunzira wina, Andireya (m'bale wake wa Simoni Petulo) anauza Yesu kuti: "Pali mnyamata pano amene ali ndi mikate isanu yabalere ndi tinsomba tiwiri, ..."

"... koma iwo ali chiyani mwa ambiri otere?" Andireya sanaone mmene chakudya chamasana cha kamnyamata kanatha kudyetsa anthu ambiri - ngakhale mnyamatayo anali wokonzeka kupereka chakudya chake kwa Yesu.



Yesu anati, "Akhazikitseni anthu pansi." Chotero amunawo anakhala pansi, chiwerengero chawo chinali ngati zikwi zisanu. Zopatsa chidwi! ZIKWI ZISANU! Amenewo sanaphatikizepo ngakhale akazi ndi ana amene anali kumeneko.



Kenako, Yesu anatenga mitanda ya mkate ndi nsombazo. Mnyamatayo ayenera kuti ankakhulupirira Yesu. Iye sankadziwa chifukwa chimene Yesu ankafunira chakudya chamasana, kapena chimene Yesu akanachita nacho. Mwina anaganiza kuti, "Ndikapereka chakudya changa chamasana, sindingathe kudya." Koma anaupereka kwa Yesu.

Kenako Yesu anapemphera. Iye adapereka takhuta kuna Mulungu. Za mikate isanu ndi nsomba ziwiri? Inde! Yesu anati "Zikomo" kwa Mulungu ndipo anamupempha kuti adalitse chakudyacho.



Atapemphera, Yesu ananyema mikate ndi nsombazo n'kuzipereka kwa ophunzira amene anagawira khamu lalikulu. Ndipamene anthu anaona chozizwitsa chimene Yesu anachita. Aliyense anadya zimene ankafuna. koma mikateyo ndi nsombazo sizinathe.

Anthu onse atadyetsedwa, panatsala mikate ndi nsomba zambiri. "Sonkhanitsani makombo kuti pasatayike kanthu," Yesu anawauza motero ophunzirawo. Iwo anadzaza mitanga khumi ndi iwiri ndi makombo a mikate isanu yabalere, imene inatsala ndi iwo amene anadya.



Tsiku limenelo, Yesu anadyetsa anthu oposa 5,000 ndi chakudya chamasana cha kamnyamata.  Nthawi inanso anadyetsa anthu oposa 4,000 ndi mikate 7 ndi nsomba zowerengeka.



Pamene anthu wamba anaona zizindikiro zimenezi, sanakwiye ngati Afarisi. M'mbuto mwace iwo alonga: "Uyu ndi Mprofeta ule anafuna kudza pa dziko yapantsi." Iwo ankadziwa kuti Yesu anali Mpulumutsi Yemwe kudza kwake kunalonjezedwa mu Mawu opatulika a Mulungu.

# Yesu Adyetsa Anthu 5,000

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Yohane 6

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16